

# UBATIZO UMAPULUMUTSA

FOR MORE INFO CONTACT;

[rdgmissions@charter.net](mailto:rdgmissions@charter.net)

[www.icotb.org](http://www.icotb.org)

Anthu ambiri owoona mtima, opembedza amakhulupirira kuti munthu amapulumsidwa ndi chisomo chokha. Ena amaphunzitsa kuti munthu amapulumsidwa ndi chikhulupiriro chokha. Magulu onsewa amakana kuti ubatizo(kumiza m'madzi) uli ndi chochita ndi kupulumutsidwa ku machimo.

**Kodi Baibulo limati chiyani? Baibulo limaphunzitsa kuti;**

1. Madalitso onse auzimu ali mwa Khristu Yesu (Aefeso 1:3);
2. Chisomo, chikhulupiriro ndi chikondi zimapezeka mwa Khristu Yesu (1Timoteo 1: 14; 2 Timoteo 2:1);
3. Chipulumutso chimapezeka mwa Khristu Yesu yekha basi ( 2 Timoteo 2:10);
4. Amene ali oyeretsedwa ali mwa Khristu Yesu (1 Akorinto1:2);
5. Moyo wosatha umapezeka mwa Yesu Khristu mokha basi ( 1 Yohane 5:11,12);
6. Ubatizo umayika munthu mwa Khristu Yesu (Agalatiya 3:27).

Aliyense wololera, woona mtima adzayenera kuvomereza kuti ngati madalitso onse auzimu, chisomo, chikhulupiriro, chikondi, chipulumutso, chiyeretso, ndi moyo wosatha zimapezeka mwa Khristu Yesu, ndiye kuti munthu ayenera kubatizidwa kuti asangalare ndi madalitso amenewa. Kukana chimenechi ndikukana mawu a Mulungu.

Baibulo silimaphunzitsa kuti ubatizo wokha umapulumsa! Komabe, limaphunzitsa kuti munthu amapulumsidwa mwa ubatizo. Anthu ampatuko amaganiza, *"iye amene akhulupirira **wapulumsidwa** ndipo **sayenera kubatizidwa.**"* Komabe Khristu Yesu adati: *"**iye amene akhulupirira nabatizidwa **adzapulumsidwa**"**(Marko 16:16). Ena amaphunzitsa, *"ubatizo sutipulumutsa."* Koma Petro mtumwi wouzidwa ndi Mulungu analemba: *"**chifaniziro chake chimene****

**chitipulumutsa ife - ubatizo"** (1 Petro 3:21)! Zomwe tiyenera kuzivomereza - chiphunzitso cha a anthu, kapena mawu a Mulungu omveka bwino( Yohane 12:48)?

Kuti munthu apulumutsidwe, amayenera kumvera Khristu Yesu (Ahebri 5:19). Tikulamuliridwa kukhulupirira (Yohane 3:16; Machitidwe 16:31). Komaso tikulamuliridwa kubatizidwa (Machitidwe 10:46). Chomcho, munthu ayenera kukhulupirira ndi kubatizidwa kuti adzapulumutsidwe. Izi ndi zoonza zenizeni zimene Ambuye Yesu adanena mu Marko 16:16: **"amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa"** . Ngati munthu akukana kubatizidwa kuti adzapulumutsidwe, akukana mawu a Mulungu!

Ndithu, munthu sapulumutsidwa ndi ntchito za kuganiza kwake(Aefeso 2:8,9; Tito 3:15), kapena sapulumutsidwa ndi ntchito za chilamuro cha Mose (Agalatiya 3:10-12). Koma munthu amapulumutsidwa pakumvera ntchito za Mulungu (Yohane 14:15; Ahebri 5:9). Chikhulupiriro ndi ntchito ya Mulungu (Yohane 6:28,29). Ubatizo ndi ntchito ya Mulungu (Marko 16:16). Mpulumutsi wachikondi yemweyo amene analankhula mawu a pa Yohane 6:28,29 ananenaso mawu a pa Marko 16:16. Ngati wina akana ichi, amakana Khristu Yesu amene adayankhulayo. Tipulumutsidwa ndi mwazi wa Khristu (Aroma 5:8). Khristu anakhetsa mwazi pa imfa yake ya pamtanda (Yohane 19:34). Tinakumana ndi mwazi wa Khristu pamene tinabatizidwa mu imfa yake(Aroma 6:3). Popanda ubatizo, munthu sangathe kulumukizana ndi mwazi opulumutsa wa Yesu Khristu. Tikane izi?

Chofunika kuti munthu apulumutsidwe ku machimo ake nchiyani?

Zimatengera **gawo la Mulungu** lomwe liri

- Chisomo (Aefeso 2:8);
- Chifundo ( Tito 3:5);
- Khristu Yesu (Mateyu 1:21);
- Moyo Wake (Aroma 5:10);
- Mwazi Wake (Aroma 5:19);
- Ndi Uthenga Wabwino wa Khristu (1 Akorinto 15:1-4).

Zimatengera **gawo la munthu** lomwe liri

- Chikhulupiriro (Aroma 5:1);
- Ntchito (Yakobo 2:24);
- Kuitana pa dzina la Ambuye (Aroma 10:13);
- Chiyembekezo (Aroma 8:24);
- Khama lathu (Machitidwe 2:40);
- Ndi kubatizidwa (1 Petro 3:21).

Baibulo silimaphunzitsa kuti munthu amapulumutsidwa ndi chiri chonse **chokha!** Mulungu, kudzera m'mawu ake, Baibulo, amati zimatengera zinthu **zonsezi** kuti tipulumutsidwe ku uchimo wathu. Kukana zoterozo ndiko kukana Mawu a Mulungu!

Kodi ubatizo umapulumutsa? **Inde, munthu ayenera kubatizidwa kuti apulumutsidwe!** Ngati mukhulupirira kuti Yesu Khristu ali mwana wa Mulungu (Yohane 8:24), ndipo muli okonzeka kulapa machimo amene akulekanitsa Inu ndi Mulungu ( Yesaya 59:1,2; Luka 13:3), ndipo muli okonzeka kuvomereza chikhulupiriro chanu mwa Khristu monga mwana wa Mulungu (Machitidwe 8:37; Aroma 10:10), ndiye bwanji osabatizidwa mwa Khristu tsopano (Machitidwe16:33)? Ngati mutero, mudzalandira madalitso onse auzimu amene amapezeka mwa Ambuye Yesu Khristu yekha